

# Vuto la Kuthamanga kwa Magazi Komanso Sitiroko

Kuthamanga magazi kokwera ndi chiopsezo chimodzi chachikulu cha sitiroko. Mlozo uwu ukufotokoza kuti kuthamanga magazi kokwera ndi chiyani, ndi kuti mungachite chiyani kuti mutsitse kathamangidwe ka magazi anu.

## **Vuto la Kuthamanga kwa magazi ndi chiyani?**

Mtima wanu umapopa magazi kupita mthupi lanu lonse kudzela mu misempha. Kuthamanga kwa magazi ndi mlingo umene umaonetsa momwe magazi amakankira misempha yanu akamadutsamo. Ngati kukankha uku kwakula kumapanikiza misempha yanu komanso mtima wanu. Ngati izi sizichepetsedwa mwa changu zitha kuchulutsa chiopsezo cha Sitiroko kapena nthenda ya mtima.

Mukapezeka ndi vuto la kuthamanga kwa magazi, zimatanthauza kuti magazi anu akhala akuthamanga kwambiri kwa nthawi yitali. Dziwani kuti nthendayi imadziwika ndi dzina la

zachipatala lotchedwa ‘Vuto la kuthamanga kwa magazi’ (High Blood Pressure).

Kayendedwe ka magazi anu kamatha kukwera kapena kutsika pa tsiku malingana ndi zomwe mukuchita pa nthawiyo, monga kupanga masewero olimbitsa thupi kapena kugona. Kusintha kwa kayendedwe ka magazi kotere kulibe kuthekela kobweretsa vuto la Sitiroko. Koma ngati kayendedwe ka magazi anu kakhala kothamanga kwa nthawi yitali katha kuwononga misempha ndipo zitha kubweretsa Sitiroko.

Vuto la kuthamanga kwa magazi ndi vuto lalikulu ku Malawi kuno.

## Kafukufuka akuonetsa kuti munthu mmodzi pa anthu akuluakulu atatu aliwonse m'Malawi muno ali ndi vuto la kuthamanga kwa magazi.

Ndi zomvetsa chisoni kuti anthu ambiri sadziwa kuti ali ndi vutoli kufikila atakumana ndi vuto lalikulu, lobwera chifukwa cha kusalandila chithandizo, zomwe zimabweretsa mavuto monga Sitiroko kapena nthenda ya mtima. Pa chifukwa chakuti vuto lakuthamanga kwa magazi lilibe zizindikilo, kuyezetsa ndi njira yokhayo yomwe mungadziwile ngati magazi anu akuthamanga kwambiri.

## Pali mgwirizano wanji pakati pa vuto la kuthamanga kwa magazi ndi Sitiroko?

### Sitoloko yodza kamba ka kuundana kwa magazi opita ku bongo (Ischaemic Stroke):

Vuto la kuthamanga kwa magazi limapangitsa kuti misempha yonse ya nthupi lanu ipanikizike, kuphatikizapo misempha yopititsa magazi ku ubongo. Kupanikizika kumeneku kumatha kuononga misempha yanu, kupangitsa kuti misempha ilimbe komanso ichepe, vuto lomwe limatchedwa 'atherosclerosis' pa chingerezi. Izi zimapeleka chiopsezo chakuti magazi aundane, zimene

zimapangitsa Sitoloko kapena kubweretsa Sitoroko ya yaying'ono chabe (Mini stroke).

### Sitoloko yodza kamba ka kutayika kwa magazi mu ubongo (haemorrhagic Stroke):

Kupanikizika kwa misempha kumene kumabwera chifukwa chakuthamanga kwa magazi kumatha kupangitsa kuti misempha ifooke ndi kuphulika mu ubongo zimene zimapangitsa kutayika kwa magazi pa minyewa yozungulira misemphayi. Izi zimatchedwa 'Haemorrhagic stroke' pa chingerezi.

### Ndi ndani amene ali pa chiopsezo cha vuto la kuthamanga kwa magazi?

Muli ndi kuthekela kwakukulu kokhala ndi vuto la kuthamanga kwa magazi ngati muli ndi chimodzi kapena zingapo mwa ziopsezo izi:

- Zaka: Chiopsezo chokhala ndi vuto la kuthamanga kwa magazi chimachuluka pomwe mukukula.
- Mbiri ya vuto la kuthamanga kwa magazi ku mtundu kwanu.
- Mtundu: Anthu akuda ali ndi chiopsezo chachikulu chokhala ndi vuto lakuthamanga kwa magazi.

- Kudya zakudya za mchere wambiri.
- Kusatakataka.
- Kunenepa kwambiri.
- Kumwa mowa mopyola muyezo.
- Vuto la kuthamanga kwa magazi limatha kuyambitsidwa ndi mavuto ena a mthupi:
- Matenda a impyo.
- Matenda a shuga.
- Vuto la kubanika popuma nthawi yogona.
- Preeclampsia - azimayi oyembekezelu amatha kukhala ndi vuto la kuthamanaga kwa magazi.
- Mavuto okhudzana ndi chitetezo cha mthupi, monga Luples
- Vuto la michere ya mthupi (Hormone problems)

Mankhwala ena amatha kusokoneza kayandedwe ka magazi mthupi monga mankhwala a kulera okumwa. Mankhwala oletsedwa agulu losokoneza bongo monga ‘cocaine’, chamba amatha kuonjezera kuthamanga kwa magazi.

## **Mgwirizano wa nkhawa ndi vuto la kuthamanga kwa magazi**

Kukhala ndi nkhawa kumatha kuonjezera kathamangidwe ka magazi mthupi kwa nthawi yochepa koma si choyambitsa chachikulu cha vutoli. Mukakhala ndi nkhawa mumatha kudya zakudya zosayenela, kumwa zoledzeletsa mopyola muyezo komanso kusowa tulo. Zinthu zonsezi zimaonjezera chiopsezo cha vuto la kuthamanga kwa magazi mthupi. Chifukwa cha ichi ndibwino kuchepetsa nkhawa ngati mbali imodzi yokhala ndi moyo wa thanzi.

## **Kuthamanga kwa magazi kumayezedwa bwanji?**

Kuyeza kuthamanga kwa magazi anu ndi kwa changu, kophweka komanso kopanda ululu ndipo kumachitidwa ku chipatala china chilichonse chachikulu, chaching’ono kapenango malo ena ogulitsilako mankhwala. Kathamangidwe ka magazi kamayezedwa pogwiritsa ntchito chipangizo cha mivi chomwe chili ndi chovala pa nkono, chopopela ndi stethoscope kapena kugwiritsa ntchito makina oyezera a digito.

## **Kutanthauzira kwa zotsatira za kuyeza kwa kathamangidwe ka magazi anu**

Kathamangidwe ka magazi anu kamalembedwa ndi manambala

awiri: Nambala yoyamba imasonyeza kukwera kwa kupanikizika komwe misempha yanu ikukumana nako pamene mtima wanu wagunda (izi zimatchedwa systolic pressure pa chingerezi). Nambala yachiwiri imasonyeza kutsika kwa kupanikizika kwa misempha yanu pomwe mtima wanu wapumila kugunda (diastolic pressure pa chingerezi). Kupanikizika kwa misempha konseku kumayezedwa mu ma millimetres a mercury omwe amalembedwa kuti 'mmHg'. Mlingo wabwino wa kathamangidwe ka magazi mmisempha ndi pakati pa 90/60 mmHg ndi 120/80mmHg. Manambala awiri onsewa ndi ofunika, ndipo kathamangidwe ka magazi kamakhala kokwera ngati imodzi kapena onse mwa manambala amenewa apyola pamenepa.

### **Vuto la kuthamanga kwa magazi limapezedwa bwanji?**

Mungapezeke ndi vuto la kuthamanga kwa magazi ngati kathamangidwe kake kakupezeka kopyola 140/90 mmHg mobwerezabwereza. Koma ngati muli ndi nthenda ya shuga, mutha kupatsidwa mankhwala ngati kathamangidwe ka magazi anu katapezeka kapyola 130/80 mmHg

mobwerezabwereza kabenanso ngati muli ndi mavuto obwera kamba ka shuga monga vuto la maso kapena impso. Asanatsimikize kuti muli ndi vuto la kuthamanga kwa magazi adokotala anu amayenera kukuyezani kangapo pakutha kwa masiku kapena masabata kuti awonedi ngati mlingowu ukukhalabe chimodzimodzi. Anthu ena amatha kupezeka ndi vuto lakuthamanga kwa magazi chifukwa cha mantha okumana ndi azachipatala. Izi zimatchedwa 'white coat effect' pa chingerezi.

### **Kathamangidwe ka magazi anu kakuyenera kuyezedwa mowilikiza bwanji?**

Anthu onse achikulire akuyenera kuyezedwa pafupipafupi. Ngati mulibe vuto yesetsani kuyezetsa kosachevela kamodzi pa chaka. Kathamangidwe ka magazi anu kakuyenera kaziyezedwa pafupipafupi (miyezi 6 ilionse) ngati kakuyandikila 140/90 mmHg chifukwa muli pa chiopsezo chachikulu chokhala ndi vuto lakuthamanga kwa magazi. Ngati munakhalako ndi mlingo okwera pa nthawi ina yake, muyenera kuyezetsa kamodzi pa miyezi 6 ilionse. Azimayi omwe akumwa mankhwala olera, oyembekezelala, Kapena omwe akumwa mankhwala othandizila michere ya mthupi (HRT)

akuyenera kumayezedwa pafupipafupi. Ndipo ngati mukumwa mankhwala othandizila kuchepetsa kuthamanga kwa magazi mthupi, mukuyenera kuyezedwa pafupipafupi monga momwe adzakulangizileni a za umoyo. Ndipo ngati mungakwanitse nkoyenera kugula ka chipangizo koyezera kathamanangidwe ka magazi kuti muzitha kuzyieza nokha kunyumba.

Ngati mukudziyeza nokha kunyumba, mudzalangizidwa kuti mudziziyeza kawiri pa tsiku; kumayambiliro ndi kumapeto kwa tsiku lanu. Ngati mukuganiza zogula makina oyelawala kambilanani ndi azaumoyo momwe makinawa angakuthandizileni kukhala ndi mlingo wa kathamangidwe ka magazi oyenera.

### **Kodi vuto la kuthamanga kwa magazi lingachepetsedwe bwanji?**

Anthu ambiri amatha kutsitsa kathamangidwe ka magazi posintha momwe amakhalira m'moyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Ngati ndinu onenepa kwambiri, kutsitsa kalemeledwe kathupi lanu kungathe kuthandiza kwambiri. Kuchita masewero olimbitsa thupi, kudya zakudya zopatsa thanzi komanso kuchepetsa kumwa mowa kungathe kubweretsa kusintha kwakukulu pakathamangidwe ka magazi anu.

Muthanso kulangizidwa kumwa mankhwala ngati muli ndi ziopsezo zina za vutoli mthupi. Kutu akuthandizeni kupanga chiganizo pa za mankhwala, adokotala amaunikira ziopsezo zomwe mulinazo zimene zitha kukupangitsani Sitiroko kapena nthenda ya mtima mtsogolo mwa moyo wanu. Amaonanso ngati vuto la kuthamanga kwa magazi layambitsa kale mavuto mthupi mwanu. Amakuyezani magazi, mikodzo komanso kagundidwe ka mtima (electrocardiogram) kuti awone ngati pali mavuto okhudza mtima.

Ngati kathamangidwe ka magazi anu kakumapezeka kopyola 140/90 mmHg mobwerezabwereza (Kapena 135/85 mmHg kunyumba) koma chiopsezo chanu cha Sitiroko chili chochepa mumalangizidwa kuti musinthe kakhalidwe ka moyo wanu wa tsiku ndi tsiku monga kutsitsa kulemela kwa thupi lanu kapena kusiya kusuta fodya.

Ngati kathamangidwe ka magazi anu kakumapezeka kopyola 140/90 mmHg mobwerezabwereza (Kapena 135/85 mmHg kunyumba) koma chiopsezo chanu cha Sitiroko ndi chachikulu, mumapatsidwa mankhwala ochepetsa kathamangidwe ka magazi komanso mumapatsidwa malangizo kuti musinthe kakhalidwe kanu ka tsiku ndi tsiku.

Ngati kathamangidwe ka magazi  
anu kakumapezeka kopyola  
160/100 mmHg  
mobwerezabwereza,  
mudzapatsidwa mankhwala  
ochepetsa kuthamanga kwa magazi,  
ngakhale chiopsezo chanu cha  
Sitiroko chili chochepa komanso  
madzapatsidwa malangizo osintha  
kakhalidwe kanu ka tsiku ndi tsiku.

### **Mankhwala a vuto la kuthamanga kwa magazi**

Pamene mwapezeka ndi vuto la  
kuthamanga kwa magazi, komanso  
mwalephera kusintha  
kathamangidwe ka magazi anu  
m'nthupi kudzera mukusintha kwa  
kakhalidwe kanu ka tsiku ndi tsiku,  
adokotala adzapanga chiganizo  
chokuyambitsani mankhwala a vuto  
la kuthamanga kwa magazi.

Pali mitundu yambiri ya mankhwala  
a vuto la kuthamanga kwa magazi  
omwe amagwira ntchito  
mosiyanasiana mthupi. Adokotala  
amapeleka mankhwala ogwirizana  
ndi zosowa zanu. Mungathe  
kupatsidwa mtundu umodzi kapena  
kuphatikiza mitundu iwiri kapena  
kuposela apo. Izi zili chonchi  
chifukwa mankhwalawa amagwira  
ntchito mosiyana, zimene  
zimapangitsa kuti agwire ntchito  
bwino ngati amwedwa amitundu  
ingapo.

Monga mankhwala ena aliwonse,  
mankhwala a vuto la kuthamanga

kwa magazi amakhala ndi mavuto  
ena otsatila mthupi nthawi zina.  
Mankhwala a vuto la kuthamanga  
kwa magazi amatha kubweretsa  
mavuto ena ngati mthupi muli kale  
mavuto ena kapena ngati mukumwa  
mankhwala ena kuphatikizapo  
ogulidwa ku golosale. Izi zikachitika,  
mukuyenera kudziwitsa adokotala  
kuti adzakuthandizeni moyenelera.  
Muyenera kudziwa kuti anthu  
ambiri samakhala ndi mavuto  
otsatila akamwa mankhwalawa.

### **Kodi mungamwe mankhwala a vuto la kuthamanga kwa magazi kwa nthawi yaitali bwanji?**

Cholina cha mankhwalawa ndi  
kutsitsa ndi kudekhetsa  
kathamangidwe ka magazi anu kwa  
zaka zambiri. Izi zimathandiza  
misempha yanu kuhala ya thanzi  
komanso kuchepetsa chiopsezo cha  
Sitiroko. Anthu ena amalangizidwa  
kumwa mankhwalawa moyo wawo  
wonse. Funifsani alangizi anu a za  
umoyo kuti akufotokozereni  
chomwe chikuyambitsa vuto la  
kuthamanga kwa magazi anu,  
komanso njira zabwino zomwe  
mungathandizikile. Musasiye  
kumwa mankhwala musanauzidwe  
kuti mutero ndi a za umoyo.

## Vuto la kuthamanga kwa magazi mu nthawi yomwe munthu ali ndi mimba

Ngati muli ndi vuto la kuthamanga kwa magazi mu nthawi yomwe mukuyembekezelala, kathamangidwe ka magazi anu kadzaunikidwa mu nthawi yoyembekezelayi, mu nthawi yomwe mukukabeleka komanso mwana akabadwa. Ngati magazi akuthamanga kwambiri mukuyenera kukhala mchipatala mpaka zitasintha. Ngati mumamwa mankhwala a vutoli musanakhale ndi pakati, mukuyenera kusintha mtundu wa mankhwala chifukwa mitundu ina siyabwino kugwiritsa ntchito mu nthawi yoyembekezelala. Mukuyenera kulankhulana ndi adokotala kuti mukambilane njira zabwino zochepetsela vuto la kuthamanga kwa magazi pomwe muli oyembekezelala.

Pomwe mwabeleka, ndikoyenela kupitiliza kuyezetsa kathamangidwe ka magazi pafupipafupi komanso kuonana ndi adokotala. Kwa anthu ena kathamangidwe ka magazi kamakhala kokwera ngakhale atabeleka ndipo akuyenera kupitiliza kumwa mankhwala a vutoli.

## Mungatani kuti mudzithandize nokha?

Kuti mudzipatse mwayi wabwino otsitsa kathamangidwe ka magazi, imwani mankhwala anu monga momwe mwalangizidwira ndi a za umoyo. Kathamangidwe ka magazi anu kaziyezedwa komanso mankhwala anu aziunikidwa pafupipafupi ndi adokotala. Adokotala anu atha kufuna kuona zimenezi pafupipafupi akangosintha mtundu wa mankhwala anu.

**Malangizo akakhalidwe ka tsiku ndi tsiku otsatirawa atha kuthandizira kutsitsa kathamangidwe ka magazi anu:**

- Chepetsani kudya zakudya za mchere ochuluka. Osamaonjezera mchere kuzakudya zanu komanso pewani kudya zakudya zokonzedwa ku ma fikitale zomwe zimakhala ndi mchere wambiri.
- Idyani magulu osachepela asanu a zipatso ndi masamba tsiku ndi tsiku.
- Tsitsani mlingo wa kulemela kwa thupi lanu ngati nkoyenera.
- Chepetsani zakumwa za gulu la khafeni (Caffeine).
- Siyani kusuta fodya.
- Chepetsani kumwa mowa ndiponso kumwa mowa mwa uchidakwa.
- Chulutsani kutakataka.
- Chepetsani nkhawa ndipo khalani ndi nthawi yopuma yokwanira.
- Yesetsani kugona ma ola osachepela 6 pa usiku uliwonse.

---

**Kuti mumve zambiri:**

Tiyimbileni ife a Stroke Support Organisation pa: 0888267713

Kapena email: [info@strokesupportmalawi.org](mailto:info@strokesupportmalawi.org)

Webusaiti: [www.strokesupportmalawi.org](http://www.strokesupportmalawi.org)

**Chilolezo chokopera ndi kukaniza uthengawu**

Chonde dziwani kuti uthenga uwu cholinga chake sikusinhanitsa ndi malangizo a akatswiri okhudza moyo wanu. Timayesetsa kuonetsetsa kuti uthenga womwe tikupereka ndi wolondora komanso watsopano, koma uthenga umatha kusintha pakadutsa nthawi. Koma momwe malamulo akulolela, Bungwe loona za matenda a sitiroko (stroke Association) silihora kukhala ndi udindo uliwonse wokhudza kagwiritside ntchito ka uthenga wa mubuku lino, kapena uthenga wochokera kwa olemba ena ndi ma website otsindikizidwa mu uthengawu.

Bungwe loona za matenda a sitiroko (Stroke Association) silitenga udindo pa zolakwika zilizone zimene zingapezeke mu chimasuliro ichi, kapena mu zotsatira za zolakwikazo. Uthenga woyambilira weniweni umene uli mu bukuli ukuyenera kutengedwa kuti ndi wolondora kufikira tsiku lozukutanso bukuli.

Bungwe loona za matenda a sitiroko (Stroke Association) ndi bungwe loyambilira ku UK pa nkhanzi za chifundo limene linadziperekwa ndi kuthana ndi nthenda ya sitiroko. Timadalira thandizo la ulere kuti tikwaniritse kuperekwa chuma ku kafukufuku wopulumutsa miyoyo ndi thandizo lina lofunikira kwa anthu amene akhudzidwa ndi matenda a sitiroko. Ngati mukufuna kumva zambiri onani Tsamba lathu la intaneti la stroke.org.uk. Kuti mupereke maganizo anu pa za bukuli lembani email ku [feedback@stroke.org.uk](mailto:feedback@stroke.org.uk).

**Chilolezo chokopera ndi uthenga wa kuzukutanso**

©Stroke Association 2018. Mlozo uwu watsindikizidwanso ndi Stroke **Support Organisation ku Malawi** ndi chilolezo chochokera ku Stroke Association. Siwukuyenera kugulitsidwa popanda chilolezo. Mlozo nambala A01F06 High Blood Pressure and stroke zamasuliridwa mu Chichewa ndi kutsindikizidwa kuno ku Malawi mu August 2024. Mlozozu udzazukutidwanso mu August 2026.

**Nambala ya mlozo : SSO 01**